




MINISTRY OF EDUCATION

PRIVATE SCHOOLS AND COLLEGES ASSOCIATION

GRADE SEVEN COMPOSITE MOCK

EXAMINATIONS-2016

NTHAWI: OLA LIMODZI

TOTAL MARKS:

1. Werengani dongosolo la macitidwe a mayeso awa mwatsatane-tsatane ndi mosamala.
2. Musatsegule tsamba ili musanauzidwe kucita tero. Aphunzitsi anu adzakuuzani nthawi yotsegula pepalali kuti muyambe kuyankha mafunso.
3. Pepala ili liri ndi mafunso okwanira makumi asanu (50) cabe mu zigawa zisanu. Muyankhe mafunso onse. Mukatsiriza kuyankha mafunso a mcigawo cimodzi, musayembekezere kuuzidwa kuti mupite kucigawo cina. Pitirizani kulemba mpaka kutsiriza mafunso onse.
4. Funso lirilonse liri ndi mayankho anai (4) amene limodzi cabe ndilo loyenera lopambana ena onse. Mukasankha yankho lanu, phimbani yankho lanu pophimba mkombero muli yankho mwasankha motere.

CITSANZO

A

B

C

Yankho lacinai 'D' ndilo lopambana onse. Conco phimbani yankho liri mu mkombero 'D'. Werengani malangizo ndi zitsanzo zonse ziri mcigawo ciriconse molingalira bwino ndiponso mosamala. Musanaphimbe yankho lanu muwerenge mayankho onse mosamala.

5. Ngati mufuna kusintha yankho mwasankha poyamba, fafanizani yankho loyamba mwaukhondo pogwiritsa nchito cofafanizira copanda dothi.
6. Musataye nthawi yaitali kufuna kuyankha mafunso obvuta mpaka potsiriza pake ngati kwakhala nthawi.
7. Ngati mwatsiriza kuyankha mafunso onse, kukatsala nthawi, gwiritsani nchito mphindi zotsalirazo kupititsamo mu mayankho anu. Onani kuti mwayankha **mafunso onse**.
8. Imikani manja anu tsopano ngati:
 - (i) muli ndi funso.
 - (ii) pepala lanu la mayankho siliri lolongosoka.

This questions paper consists of 11 pages.

CIGAWO COYAMBA

Malangizo

Funso lirilonse liyamba ndi ciganizo ciri ndi liu kapena dera lina losowa m'malo amene aonetsedwa. Munsi mwake mudzapezamo mau kapena madera a ziganizo anai. Liu limodzi mwa anai ndilo litsiriza bwino coganizo.

Citsanzo: Mnyamata aliyense ali ndi kakhasu kobzalira mtedza.

- A. kanga
- B. langa
- C. kake
- D. yake

Yankho "C" kake, ndilo liu litsiriza bwino coganizo conse. Conco munakaphimba yankho "C" mu mkombero motere.

A	B		D
---	---	--	---

Tsopano yankhani mafunso otsatira:

1. Taphika kale nsima _____ palibe ndiwo.
A. koma B. cifukwa C. kapena D. ndipo
2. Dziko la USA linalandira ufulu wodzilamulira _____ 1776.
A. pa B. ku C. ndi D. mu
3. Roisi wabvala delesi _____ yera.
A. wo B. ko C. co D. lo
4. Bikkiloni _____ Diffikoti amacita sewero pa Muvi TV.
A. onse B. ndi C. pamodzi D. na
5. _____ mwana anaona amai ake anayamba kulira.
A. Nanga B. Ngati C. Cifukwa D. Pamene
6. Mvuu inagwera pamadzi kuti _____ !
A. seepee B. buli C. faa D. phavaa
7. _____ kuti wabvala zabwino, iye sanasambe.
A. Nanga B. Ngati C. Ndipo D. Ngakhale
8. Caka cino _____ ndi masankho mziko lanthu.
A. timakhala B. tidzakhala C. tikukhala D. tidzakakhala
9. _____ dzina langa ndine Chenjerani Phiri.

A. Ine
Iwo

B. Inu

C. Iye

D.

10. Deliya ndi Mtsikana _____ kongola.

A. co

B. ko

C. wo

D. yo

11. Amai anena _____ tisapite kumunda lero.

A. ati

B. anati

C. kuti

D. mwina

12. Baibulo _____ ndi uthenga wocokera kwa Mulungu.

A. ali

B. liri

C. ndi

D. uli

13. Tsirizani mwambi uwu moyenera, "Nyama yaliuma _____"

A. inapulumuka kunkhondo

C. inafa ndi ludzu

B. inathawa antu Osaka

D. inagwera m'mbuna

14. Mungathe kulima thonje _____, cimanga m'munda uwu.

A. cifukwa

B. ndipo

C. mwina

D. kapena

15. Sankhani ciganizo coyenera:

A. Zimene wanena awa wanthu ndi zoona

B. Zimene anena anthu awa ndi zoona

C. Zamene anena awa anthu ndi zoona

D. Zameme inena awa wanthu ndi zoona

CIGAWO CACIWIRI

Malangizo

M'cigawo ici, funso lirilonse liri ndi ciganizo comwe sicinaikidwe zopumira.

M'malo onse amene mufunika zopumirazi mwaikidwa manambala. Munsi mwa ganizo lirilonso mudzapezamo njira yosonyezera kaikidwe ka zopumira m'malo muli manambala muja.

Cistanzo: Amai andipatsa mpeni (1) nkhwangwa (2) khasu (3) ndi mpiri (4) ndipita nazo kumunda.

	1	2	3	4
A.	!	,	.	,
B.	,	,	.	,
C.	,	,	.	.
D.	.	.	,	.

Yankho 'C' ndilo loyenera

Tsopano pakuyankha funso papepala lanu la mayankho, mukanaphimba mkabokosi momwe muli lembo **"C"** motere.

A	B		D
---	---	--	---

Tsopano yankhani mafunso otsatira:

16. Mwadzuka bwanji ana inu (1) Ine ndiribwino Khalani pansi (2) Lero tidzaphunzira masamu akuchulukitsa (3) Kodi zinthu zimaculuka (4)

1 2 3 4

- A. , , , .
 B. ! . . !
 C. ! . . ?
 D. ? ! ? .

17. Kalekale (1) nkhandwe inagwidwa mu msampha ndipo pofuna kucoka mumsamphamo inaduka mcira (2) pozindikira kuti siinali kuoneka bwino ndi mcira waufupi (3) inaganiza zoitanitsa msonkhano niiuza anzake kuti adule micira yawo ndipo adzaoneka bwino ngati adzacita tero (4)

1 2 3 4

- A. , . , .
 B. . , , .
 C. , , , .
 D. ! , , ?

18. Ana inu (1) kodi mudziwa kusiyana kulipo pakati pa mbewa ndi khoswe (2) mbewa ndi yoyera kumimba koma khoswe ndi wakuda (3) mbewa imakhala kuchire koma khoswe amakhala m'mudzi kapena m'tauni ndipo anthu amadya mbewa osati khoswe (4)

1 2 3 4

- A. , ? . .
 B. ! ! ? ?
 C. ? ! ! .
 D. , , , .

19. Fulu ndi nkhozi ndi nyama zodabwitsa (1) izo zilibe malo mokhala mwenimweni (2) komabe (3) zimayenda ndi nyumba zawo kulikonse kumene zipita (4)

1 2 3 4

- A. ! ? ! ?
 B. . , , .
 C. , , , .
 D. ? ! , .

20. Ng'ona ndi buluzi wamkulu amene amakhala m'madzi (1) kodi maonekedwe ake muwadziwa bwino (2) maonekedwe a cilombo cimeneco ndi oipa ndipo mamba ake salinso bwino ayi (3) mutu ndi maso ake ndi owopsa kwambiri (4)

1 2 3 4

- A. , . , .

- B. . ? ! .
 C. ! ? ? ?
 D. . ? . .

CIGAWO CACITATU

Malangizo

M'cigawo ici, funso lirilonse liri ndi ziganizo ziri ndim manambala osaikidwa mu m'ndandanda wabwino. Ikani ziganizo izi mu m'ndandanda wa dongosolo labwino kuti zonedwa zones kinhalke zomveka.

Werengagani ziganizo zonse mosamala ndi kusankha njira yolongosoka motsatira manambala kuti zikhale mu dongosolo lomveka bwino.

- Citsanzo:**
- | | |
|---|--|
| 1 | Kodi ndimwe munthu wa mtundu wanji |
| 2 | Sitidzayenda nawenso kuyambira lero |
| 3 | Wosafuna kudzisamalira |
| 4 | Umangoticititsa manyazi pagulu la atsikana |

- | | | | | |
|----|---|---|---|---|
| A. | 4 | 3 | 1 | 2 |
| B. | 3 | 2 | 4 | 1 |
| C. | 1 | 3 | 4 | 2 |
| D. | 2 | 4 | 3 | 1 |

Yankho “C” ndilo lolongosoka mu m'ndandanda. Nkhani yonse iyenera kukhala tere:

A	B		D
---	---	--	---

- | | |
|---|--|
| 1 | Kodi ndimwe munthu wa mtundu wanji |
| 3 | Wosafuna kudzisamalira |
| 4 | Umangoticititsa manyazi pagulu la atsikana |
| 2 | Sitidzayenda nawenso kuyambira lero |

Tsopano yankhani mafunso awa:

21. 1. Koma podzafika pa January 9, 2011, anthu a dzikolo anali ndi Referendum ndipo zotsatira
 zake n'zakuti
2. padzakhala maiko awiri, North Sudan ndi South Sudan kuyambira pa July 9, 2011.
3. Dziko limenelo linalandira ufulu wodzilamulira mcaka ca 1956 kucokera ku maiko a Egypt ndi Britain.
4. Dziko la Sudan ndi dziko lalikulu kuposa mu Africa ndipo likulu lake liri ku Khartoum.

- | | | | | |
|----|---|---|---|---|
| A. | 1 | 2 | 3 | 4 |
| B. | 2 | 1 | 4 | 3 |

- C. 4 3 1 2
D. 4 3 2 1

22. 1. Kalekale panali Mkango umene unali kudwala
2. Unabvutika kwa nthawi yaitali, koma tsiku lina Fisi anabwera ndi kuuza Mkangowo kuti Kalulu
 anali kudziwa mankhwala a matenda ake.
3. Pamene Kalulu anafika kunyumba ya Mkango, anabvomera kuti anali kudziwadi mankhwala
 koma cizimba ca mankhwala akewo cinali mtima wa Fisi.
4. Fisi iye anathawa nthawi yomweyo atamva mau a Kalulu

- A. 1 2 3 4
B. 1 3 4 2
C. 2 3 4 1
D. 2 4 1 3

23. 1. Kuti muntu akhale ndi thanzi labwino ayenera kudya cakudaya ca magulu atatu
2. Pali mitundu yambiri ya cakuday koma
3. magulu atatu a cakudaya ndi zakuday zopatsa mphamvu, zakuday zomanga thupi ndi zakuday
 zoteteza thupi.
4. Kodi inu mumadya zakuday za magulu atatu izi?

- A. 4 1 2 3
B. 1 4 2 3
C. 1 2 3 4
D. 2 1 3 4

24. 1. Podzafika pa July 6, 1964 Nyasaland anadzakhala Malawi ndipo pa October 24, 1964 Northern Rhodesia anadzakhala Zambia.
2. Kucokera m'caka ca 1953 kudzafika mu 1963 maiko a Malawi, Zambia ndi Zimbabwe
 amalamulidwa ndi Britain.
3. Ndipo maiko onse atatu amachedwa kuti Federation of Rhodesia ndi Nyasaland.
4. Ndiposo pa April 18, 1980 Southern Rhodesia anakakhala Zimbabwe.

- A. 1 2 3 4
B. 4 3 2 1
C. 2 3 1 4
D. 3 2 4 1

25. 1. Ana inu, kodi mudziwa bwino dziko la Zambia? Dzikoli ndi lalikulu mtunda wa makilomita

752,600 monsemonse.

2. Likulu lake liri ku Lusaka, ndipo kumeneko kuli Nyumba ya Malamulo.

3. Liri ndi zigawo zisanu ndi zinai; cigawo cacikulu kwambiri ndi Northern Province ndipo

4. cigawo cymene ciri ndi Cuma kwambiri ndi cigawo ca Copperbelt Province ndipo cigawo ca

Western Province ciri ndi Cuma cocepa.

- | | | | | |
|----|---|---|---|---|
| A. | 4 | 3 | 2 | 1 |
| B. | 4 | 2 | 1 | 3 |
| C. | 1 | 2 | 4 | 3 |
| D. | 1 | 2 | 3 | 4 |

26. 1. Koma pamene Ng'ona inanva za nkhaniyo inacenjeza ana ake kuti asakapitekonso kumtsinje

kuja cifukwa Mkango ungawadye.

2. Tsiku lina ana awiri a Ng'ona anapita kukasewera kumtsinje

3. Kumtsinjeko anakomanako ndi ana awirinso a Mkango

4. M'madzulo ana aja anauza makolo awo zimene anaona tsikulo

- | | | | | |
|----|---|---|---|---|
| A. | 1 | 2 | 3 | 4 |
| B. | 2 | 3 | 4 | 1 |
| C. | 1 | 2 | 4 | 3 |
| D. | 4 | 3 | 2 | 1 |

27. 1. Mwenye poona concho anampitikitsa pa nchito

2. Iye anayamba ucidakwa ndikulephera kupita kunchito

3. Mulungu anamdalitsa ndipo anapeza nchito yogulitsa musitolo la mwenye

4. Tembo anapita ku Chipata kukafuna nchito

- | | | | | |
|----|---|---|---|---|
| A. | 1 | 2 | 3 | 4 |
| B. | 4 | 3 | 2 | 1 |
| C. | 4 | 3 | 1 | 2 |
| D. | 4 | 3 | 2 | 1 |

28. 1. Munthu amene ali ndi kacilombo ka HIV mthupi lake

2. umoyo wake ungapite patsogolo ngati akuday zakudaya zabwino ndiponso apewa khalidwe la

dama kapena la ciwerewere.

3. koma ayenera kudziwa kuti

4. akhoza kukhala zaka zambiri ndikachilombo kameneko mthupi lake wosadwala Edzi.

- A. 1 4 3 2
 B. 1 4 2 3
 C. 1 3 2 4
 D. 1 2 4 3

29. 1. Jeneti anapita kuti amlembe nchito
 2. Mzungu anamuuza kuti afuna wanchito woziwa kulankhula cizungu
 3. Mzungu anali kufuna mlezi wan ana ake
 4. Jeneti sanamlembe nchito cifukwa analephera kulanhula cizungu

- A. 4 1 3 2
 B. 4 3 2 1
 C. 3 1 2 4
 D. 1 3 2 4

- 30.1. Mphunzitsi anayankha nati nauka bwino zikomo khalani pansi
 2. Mphunzitsi anapatsa aphunzi moni mkalasi nati mwauka bwanji nonse
 3. Aphunzi anayankha nati, tauka bwino kaya inu mphunzitsi
 4. Aphunzi onse anakhala pansi

- A. 2 3 4 1
 B. 2 1 4 3
 C. 2 3 1 4
 D. 2 4 3 1

CIGAWO CACINAI

Malangizo

M'cigawo ici, mudzayesedwa ngati mungathe kudziwa matanthauzo a mau madera a ziganizo kapena ziganizo zomwe. Munsi mwa funso liri lonse muli mayankho anai. Yankho limodzi cabe ndilo lopanbana ena onse. Phimbani yankho mwasankha monga mwasonyezedwa pansipa.

Citsanzo: Tikati Belita **wapsya mtima** ndiko kuti

- A. anathenda mtima
 B. mtima wake unali pamoto
 C. mtima wake unapsya ndi moto
 D. wakalipa kwambiri

Yankho "D" ndilo loyenera

A	B	C	D
---	---	---	---

Tsopano yankhani mafunso awa:

31. Patsiku loweruka Dorofi anabvala **dekesha**. Liu lakuti ndekesha lithanthauza

- A. citenje cacitali C. delesi lalitali

- B. citenje copanda utoto D. delesi lalifupi
32. Tikanena kuti Abambo Daka ndi a **mbutuma** titanthauza kuti iwo ndi ____
 A. munthu wopusa C. munthu wakuba
 B. munthu wocenjera D. munthu wosokonezeka
33. **Ukanapita** kuchire ukanaiona njoka yamtundu wa nsato.
 Ciganizo ici citanthauza kuti muntuyo ____
 A. Anapita kuchire ndipo anaona nsato C. Sanapite kuchire ndipo sanaione nsato
 B. Anapita kuchire koma sanaione nsato D. Sanapite kuchire koma kunalibe nsato
34. M'banja la a Phiri, Belita ndi **nchowa**. Liu lakuti nchowa lithanthauza ____
 A. mwana wamwamuna woyamba kubadwa
 B. mwana wamkazi woyamba kubadwa
 C. mwana wamwamuna wotsiriza kubadwa
 D. mwana wamkazi wotsirizira kubadwa
35. Mau akuti **Debora ndi njoka** atanthauza kuti iye ndi ____
 A. wantima woipa C. wamutali ngati njoka
 B. wantima ngati njoka D. wamfupi ngati fulu
36. Nyumba ya wailesi yakanema ya Muvi Television **imaulutsa** zithunzi zokondweretsa. Liu **kuulutsa** litanthauza ____
 A. kufalitsa B. kutumiza C. kunena D. kukalipa
37. Ngati munthu wina ali ndi **cisoni**, ndiye kuti munthuyo ali ndi ____
 A. nsanje B. kaduka C. cidani D. cifundo
38. Tikanena kuti Amai Lungu ndi **cumba** titanthauza kuti iwo ndi ____
 A. mzimai amene sabereka C. mwamuna amene sabereka
 B. mzimai amene abereka kwambiri D. mwamuna amene abereka kwambiri
39. Ngati munthu wina ndi **waliuma** ndiye kuti iye ndi ____
 A. wabwino mtima C. wosamvera za anzake
 B. wosalimba thupi D. wokongola thupi
40. M'nyengo ya **Chisanu** tiyenera kubvala zobvala zofunda. Liu **Chisanu** litanthauza ____
 A. nthawi yotentha kwambiri C. nthawi yamkutho kwambiri
 B. nthawi yamvula kwambiri D. nthawi yozizira kwambiri

CIGAWO CACISANU**Werengani nkhani iyi ndipo muyankhe mafunso otsatira.****Nkhani yoyamba (1)****NCHITO ZA MOTO**

Moto ndi bwenzi labwino kumtundu wa anthu. Pali nchito zambiri zimene zimafuna moto monga kuphikira, kuochera zitsulo, kuochera zinthu zoumbidwa ndi dothi la kumtapo ndi kufunditsira madzi osamba. Nthawi zina ngati kwazizira, timaotha moto kuti tifunditse mathupi athu. Ici n'cifukwa cake anthu ambiri amabvala zobvala zothuma kuti zifunditse magazi awo mthupi.

Anthu ena amaopa moto cifukwa cakuti moto ukauluka ungaphe munthu. Makanda ndi anice ang'ono amakonda kuseweta pafupi ndi moto. Ngati ana amenewo asewera pafupi tero, iwo angagwere m'moto mmenemo kapena angagwetse mbaula ndipo moto ungataiyike ndi kucita n'gozi. Kucita masewera pafupi ndi moto sibwino ayi cifukwa cake makolo ena **samalola** kuti ana awo aziotha moto ngati kwazizira

Kutseka mazenera pootha moto mnyumba sibwino ayi. Anthu ena amalephera kupuma cifukwa ca utsi woipa wocokera ku **makala** a pambaula. Conco, njira yabwino koposa yogwiritsira nchito moto ndi kusegula mazenera pootha moto mnyumba. Ngati titsatira njira ziwiri izi, ndiye kuti moto udzapitirizabe kukhala bwenzi labwino.

Tsopano yankhani mafunso awa

41. Kodi ndi nchito zingati za moto zimene zachulidwa m'nkaniyi?

- A. ziwiri B. zitatu C. zinai D. zisanu

42. Makanda ndi ana ang'ono sayenera kusewera pafupi ndi moto cifukwa ____

- A. adziwa kuphika m'zikopo C. angacite ngozi ndi moto
B. angaphike nsima yaiwisi D. adziwa kupewa ngozi

43. Liu lina limene lifanana mdi **malasha** ndi _____

- A. makala B. nkhuhi C. moto D. ndowe

44. N'cifukwa ciani sitienera kutseka mazenera ngati mbaula ya moto iri mnyumba?

- A. kuti mpweya woipa usatuluke munyumbamo
B. kuti mpweya woipa utuluke munyumbamo
C. cifukwa kungazizire kwambiri
D. cifukwa kutentha sikungakwane bwino

45. Kumalo kumene anthu amatenga dothi ndi _____

A. kucishala

B. kumtapo

C. kucungu

D. kutsindwi

Nkhani Yaciwiri (2)**MFUMU MKANGO AKWIYA**

Mfumu Mkango anakondwera kwambiri pamene mkazi wake, **anabereka** mwana. “Nyama zonse zamchire ziyenera kubwera ndi kusangalala nane panthawi yabwino zedi ya moyo wanga. “Unatero mfumu Mkango mumtima.

Mfumu inaitana mthenga wake wamkulu ndipo anam’tuma uthenga woti akauze nyama zina. Koma **Nyalugwe** anacita ulesi wakuti auze aliyense, conco anaganiza za njira yosabvuta. “Ndidzauza munthu wina kuti akapereke uthenga kwa munthu wokhala pafupi. M’njira iyi, nyama zonse zamchire zidzalandira uthenga. “Anaganiza tero Nyalugwe pamene anali kupita kunyumba ya mbidzi.”

Pamene Nyalugwe anafika panyumba anapeza Mbidzi iri mtulo ndipo anaiuza uthenga. Itauka mbidzi, inakumbukira kuti iyenera **kutumiza** uthenga, conco, inafulumira kupita kunyumba ya Ng’ona.

Ngoma inali kusamalira mwana wake wodwala. Cifukwa cakuti Ngoma inalu kuona mwana wodwala, siinamvetse bwino uthenga umene Mbidzi inabweretsa. Pamene Mbidzi inabwerera kwao Ng’ona inakumbukira kuti unali ndi uthenga woti itumize, koma inaiwala uthenga wake. Inapita kunyumba ya Njati kumuuzza uthenga wosiyana ndi umene anauzidwa. Umu ndi mmene uthengawo unafikira nyama zonse.

Tsiku lacikondwerero litafika, nyama zina zinabweretsa mphatso za zipatso ndi nyama , zinsano zinanyamula makasu ndi nkwangwa . Nyama zina zinabvala zobvala za kumaliro a mfumukazi mkango. Nsato, Fisi ndi Bvumbwe ananyamula zida zosakira nyama.

Njobvu inabwera m’mamawa kwambiri kuti idzasankidwe Mfumu yatsopano, cifukwa anauzidwa kuti mkango unali utafa.

Mfumu Mkango anakwiya kwambiri ndi uthenga wake.

Tsopano yankhani mafunso otsatira

46.Kodi ndani amene anali Mfumu yanyama?

A. Nyalugwe

B. Mkango

C. Njobvu

D. Njati

47. Ngoma siinamvetse uthenga wa Mfumu cifukwa _____

A. mwana wake anali wodwala

B. mwana wake anali kuchita phokoso

C. inamvetsera bwino pamene uthengawo una perekedwa

D. inali yodwala kwambiri

48. Nyama imene inapereka uthenga wolakwika poyamba inali ____
 A. Mbidzi B. Nyalugwe C. Ngoma D. Mkango

49. Uthenga umene Nyalugwe anauzidwa unali wakuti ____
 A. Njati yabereka mwana wa Mkango
 B. Fisi wabereka mwana wamkazi wa munthu
 C. Mkango wabereka mwana wa galu
 D. Mfumukazi Mkango wabereka mwana wathanzi lawino

50. Mthenga wa Mfumu Mkango anali ____
 A. Nyani B. Nyalugwe C. Njati D. Njobvu

Mayeso anu atha